

Phunziro 3, April
19, 2025

ZITHUNZI ZOCHOKERA MU UKWATI



“Kenaka mngelo
anandiwuza kuti,
“Lemba kuti,
Odala amene
ayitanidwa ku
phwando la ukwati
wa Mwana
Wankhosa.”
Ndipo anatinso,
“Awa ndiwo mawu
woona a Mulungu’
”



Chivumbulutso 19:9



Kawirikawiri, mu Chipangano Chakale ndi Chatsopano, anthu a Mulungu amafaniziridwa ndi mkazi kapena mkwatibwi.

Nthawi zina timaona ngwirizano umenewu ukuonetseredwa mu maukwati amene akazi awo anali okhulupirika (monga Rebeka) kapena osakhulupirika (monga Goma)

Nthawi zina, zizindikiro za akazi okhulupirika (mkwatibwi wa Mwanawankhosa) kapena akazi achigololo (Babuloni Wamkulu) zimagwiritsidwa ntchito mwachindunji.



Zizindikiro mu ukwati.



Akazi osakhulupirika:



Msungwana wosiidwa.



Mkazi wa Hoseya.



Babuloni Wamkulu.



Akazi okhulupirika :



Rabeka.



Mkwatibwi wa Mwanawankhosa.

ZIZINDIKIRO MU UKWATI

“Chifukwa chotero mwamuna adzasiya atate wake ndi amake nadzadziphatika kwa mkazi wake: ndipo adzakhala thupi limodzi” (Genesis 2:24)

Pamene Mulungu analenga anthu, anawapatsa mphatso ziwiri: Sabata (Genesis 2:2-3) ndi ukwati (Genesis 2:24). Zonsezi zimakhudza ubale: ubale wathu ndi Mulungu, komanso ubale pakati pa mwamuna ndi mkazi.



Mu ungwiro wake, ukwati unkasonyeza ubale wangwiro pakati pa Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera. Chifukwa cha tchimo, umayimira mgwirizano pakati pa Mwamuna wangwiro—Yesu—ndi Mkazi opanda ungwiro—Mpingo (Aefeso 5:31-32)

Mu Baibulo lonse timawona mmene amuna amayetsesera kusintha akazi awo kuti akhale abwino kwambiri ndipo kupeza chikondi chawo. Kuchokera pa chitsanzo ichi cha ukwati, ifenso tingaphunzire momwe tingachitire m'mawukwati athu—pakati pa anthu awiri osakwana):

Khululukirani
nzanu wa ukwati,
ngakhale ali
osayenere



monga momwe
Khristu
amatikhulukira,
ngakhale tiri
osayenera

Lolerani mzanu wa
ukwati, limodzi ndi
zofooka zake zonse



monga momwe
Khristu amatilolera
ife, limodzi ndi
zofooka zathu zonse

Ikani mzanu wa
ukwati patsogolo
panu



monga momwe
Khristu anaikira
patsogolo pa
iyemwini



AKAZI OSAKHULUPIRIKA

MSUNGWANA WOSIIDWA

“Tsono pamene ndinkadutsanso ndinaona kuti nthawi yako yomanga banja inakwana. Tsono ndinakufunditsa chovala changa ndi kubisa umaliseche wako. Ndinachita nawe pangano la ukwati ndipo unakhala wanga, akutero Ambuye Wamphamvuzonse” (Ezekieli 16:8)







M’masomphenya ake, Ezekieli anasonetsedwa mmene Mulungu anapezera mwana wa mkazi wakhanda wosiidwa (Israeli); anamupatsa moyo; namuthandiza kukula; anapanga naye pangano la ukwati; ndipo iye anakhala mfumukazi ndi kuyamikiridwa ndi onse (Ezekieli 16:1–14.)

Izi zikufotokoza mwachidule nkhani ya chikondi pakati pa Mulungu ndi Aisraeli, kuyambira kutuluka kwawo ku Igupto kufikira nthawi ya ulamuliro wopambana wa Davide ndi Solomoni, pamene Israeli ankayamikidwa ndi mitundu yonse (1 Mafumu 10:1.)


Koma Israeli anaiwala kuti kukongola kwake kunali mphatso yochokera kwa Mulungu, chiwonetsero cha kukongola kwaumulungu (Ezekieli 16:14), ndipo anapatuka kwa Mwamuna wake, kuchits chigololo potsatira milungu ina (Ezekieli 16:15–17.)

Tinalengedwa kuti tizionetsa ubwino ndi ulemerero wa Mulungu. Pamene tikaganiza kuti ubwino wathu umachokera mwa ife eni, pomwepo mavuto amayamba.



MKAZI WA HOSEA

"Yehova atayamba kuyankhula kudzera mwa Hoseya, Yehova anati kwa Hoseyayo, "Pita kakwatire mkazi wachiwerewere ndipo ubereke naye ana m'chiwerewere chake pakuti anthu a m'dziko muno achimwa pochita chigololo choyipitsitsa, posiya Yehova (Hosea 1:2)





Kuyambira pachiyambi, Mulungu anafotokoza momveka bwino kuti lamulo limene anali atazipereka kwa Hoseya lakuti akwatire Goma (amene anadzipereka kuchigololo ndi kusiya mwamuna wake) linali chizindikiro cha ubale pakati pa Mulungu ndi Israeli (Hoseya 1:2)

Hoseya anagwiritsa ntchito njira zosiyanasiyana kuti abwezeretse chikondi cha mkazi wake (Hoseya 2:6–7, 14–15). Popeza njira zimenezi sizinagwire ntchito, anafunika kulipira dipo lake (Hoseya 3:2–3).

Zachidziwikire, chipulumutso chathu chinatengera Mulungu mtengo woposa "zidutswa zasiliva khumi ndi zisanu, komanso theka la barele

Tsoka ilo, Mpingo unatsatiranso njira yolakwika yomweyo monga anachitira Israeli. Koma chikondi cha Mulungu sichinasinthe (Hoseya 11:4). Iye akupitiriza kutipempha kuti tisiye "chigololo chathu" ndipo tibwerera kwa Iye (Hoseya 14:1–2; Chivumbulutso 18:2–4)



BABULONI WAUKULU

“Pa mphumi pake panalembedwa dzina lodabwitsa: BABULONI WAMKULU
MAYI WA AKAZI ADAMA NDI WAZOYIPITSA ZA DZIKO LAPANSI” (Chivumbulutso 17:5)

Kodi Babuloni ndi ndani kapena chiyani?

Mkazi woyera amaimira anthu a Mulungu okhulupirika (Chivumbulutso 12:1; Aefeso 5:25–27). Koma Babuloni, mayi wa achigololo, amaimira anthu a Mulungu amene amusiya ndikumadalira mafumu a dziko lapansi (Chivumbulutso 17:1–5.)

Kusakhulupirika kwa anthu Ake kumapangitsa Mulungu chisoni chachikulu. Kwa zaka zambiri, wakhala akuyesetsa kubwezeretsa Mpingo wake mu chiyero, koma ochepa ndi amene ayankha. Pomaliza, adzapereka pempho lake lomaliza (Chivumbulutso 18:4.)



Potsatira kukhulupirika, ubwenzi ungathe kubwezeretsedwa. Koma, mwatsoka, nthawi zina zimafika pokwana, pamene kubwezeretsaana sikungatheke.


Nthawi idzafika imene Babuloni ndi onse amene atsala mwa iye adzaweruzidwa ndi kulangidwa (Chivumbulutso 19:1–5). Koma okhulupirika, a mkwatibwi wa Mwanawankhosa, adzakhala ndi moyo kosatha pamodzi ndi Yesu (Chivumbulutso 19:6–8.)



AKAZI OKHULUPIRIKA

REBEKA

“Choncho iwo anamuyitana Rebeka uja namufunsa kuti, “Kodi ukufuna kupita ndi munthuyu panopa?” Iye anayankha kuti, “Ndipita” (Genesis 24:58)



Malinga ndi mwambo wa munthawi yake, Abrahamu anapita kukafunsira mkazi wa mwana wake, Isake. Koma sanafune kuti mwana wake akwatire mkazi aliyense wa ku Kanaani, koma akwatire mmodzi mwa abale ake, amene anali kutali kwambiri, mitunda mazana (Genesis 24:2–3)

Cholinga cha izi? Ngakhale abale ake sanali angwiro, iwo ankalambira Mulungu wona, pamene Akanani ankamukana. Isake akanakwatira mkazi wa ku Kanaani, moyo wake wauzimu ukanalowa pansi chifukwa cha mphamvu ya zochita zoyipa za mkaziyo.

Iyi yakhala ndi mbiri ya Mpingo pamene ulowa mu “maukwati” ndi mitundu ya dziko lino. Pang’onopang’ono, Mpingo wapatuka kuchoka mu chikhulupiriro choona.

Chinthu china chapadera munkhaniyi ndi chakuti Rebeka anafunsidwa ngati akufuna kukwatiwa, pomwe malinga ndi mwambo wa nthawi imeneyo, analibe ndi mwayi wosankha (Genesis 24:50–51, 57–59).)

Kukhala m’gawo la mkwatibwi wokhulupirika wa Mulungu ndi chisankho cha mumtima. Tiyeni tivomereze chikondi cha ndi mawu omveka bwino, “Ndidzapita.”



MKWATIBWI WA MWANAWANKHOSA

“Tiyeni tisangalale ndi kukondwera ndi kumutamanda! Pakuti nthawi ya ukwati wa Mwana Wankhosa yafika, ndipo Mkwatibwi wakonzekeratu” (Chivumbulutso 19:7)

Chozizwitsa choyamba cha Yesu chinachitika pa ukwati (Yohane 2:1-11). Kwa ife, chochitika ichi chili ndi chizindikiro chapadera chimene chimatithandiza kumvesetsa Dongosolo la Chipulumutso.

Mwina chofunikira kwambiri ndi chakuti, kuti mkwatibwi (ife) akhale wokonzeka, amafuna vinyo amene Yesu amapereka, ndiwo, mwazi wake oyera otsuka (Yohane 2:6; Chivumbulutso 7:14)

Yesu anagwiritsanso ntchito fanizo la ukwati kufotokoza zinthu zina zokhudza kukonzekera kubwera kwake posachedwa. M’maganzizo onse amenewa, mkwatibwi samatchulidwa, koma alendo a ku ukwati. Kodi alendo amenewa angakhale mkwatibwi mwiniwake?

Kodi tingaphunzire chiyani kuchokera mu mafanizo amenewa?

- ❖ Kukhalani ndi Mzimu Woyera
- ❖ Vomerani kuitanidwa kwanu


Anamwali khumi (Mateyu 25:1-13)



❖ Aliyense ali oyitanidwa ku ukwati

❖ Tiyenera kuvala Khristu

Alendo osayenera (Mateyu 22:1-14)



“Khristu wakhala mnzawo wa tsiku ndi tsiku komanso bwenzi loyandikana nalo. Iwo akhala moyo oyandikana ndi kulumikizana kosalekeza ndi Mulungu. Pa iwo, ulemerero wa Ambuye wawunikira. Mwa iwo kuunika kwa chidziwitso cha ulemerero wa Mulungu pankhope ya Yesu Khristu kwawonekera. Tsopano akusangalala mukuwala kosazimirira kpma kowoneka bwino ndi ulemerero wa mfumu mu ukulu wake. Iwo ali okonzeka kulowa mu ngwirizano wa kumwamba; pakuti amalingalira za kumwamba mumtima mwawo.”